Kodi ndi zinthu ziŵiri zotani zimene tiyenera kugonjetsa nazo mayesero?

(1) ______________________________________________

(2) ______________________________________________

==================================================================

SABATA LACHITATU: KHRISTU AKONZEKERA NTCHITO YAKE
TSIKU LACHISANU: KUBWEREZA

Tsopano mwatsiriza maphunziro a sabata zitatu. Mwakhala mukugwira ntchito molimba. Mwaphunzira moyo wa Khristu kufikira pa nthaŵi yamayesero ake. M'gawo limeneli atsiriza zaka makumi atatu zoyamba za moyo wake.

Tsopano tiyeni tibwereze zinthu zimene mwaphunzira. Yesetsani kuyankha mafunso onse aphunziro ili. Musayang'ane kumbuyo kwa bukuli kuti muone mayankho kufikira mutalemba yankho lililonse. Pamene mwatsiriza, bwererani pamapeto a phunziro lililonse. Onani ngati mwayankha bwino, ngati yankho lanu ndi lolakwika iphani ndi mzere. Ndipo lembani lolondola pamwamba pake.

MAFUNSO OCHOKERA KU SABATA LOYAMBA:

1. Lembani zolinga ziŵiri zophunzirira moyo wa Khristu.

   (1) ______________________________

   (2) ______________________________

2. Kodi Khristu asanabwere m'dziko lapansi anali kuti?

   ______________________________

3. Kodi Khristu anali ndani asanadze m'dziko lapansi?

   ______________________________

4. Kodi chinthu chodabwitsa kwambiri pa za kubadwa kwa Yesu Khristu ndi chiyani?

   ______________________________

5. Kodi kubadwa kwa Yesu kunasiyana motani ndi kubadwa kwa anthu ena?

   ______________________________

6. Kodi Mariya namwaliyo anaona mwana ndi mphamvu ya yani?

   ______________________________

7. Lembani chifukwa chimene angelo anapatsira maina aŵa kwa Yesu.

   (1) Mpulumutsi ______________________________

(2) Khristu - ______________________________

(3) Ambuye - ______________________________

==================================================================

MAFUNSO OCHOKERA MU SABATA ŁACHIŴIRI:

8. Mphatso za anthu anzeru zimatikumbutsa ife kupereka kwa Yesu.

(1) Mmalo mwa golidi wa mfumu, kodi tikhoza kupereka chiyani?

______________________________

(2) Mmalo mwa Libano wa Mulungu, kodi tikhoza kupereka chiyani?

______________________________

(3) Mmalo mwa Mure wa Mpulumutsi wofera, kodi tikhoza kuperekanji?

______________________________

9. Kodi ndi chifukwa chiyani Satana ankafuna kupha Yesu kupyolera mwa Herode?

______________________________

______________________________

10. Kodi nt[illegible] ya Herode ndi khanda Yesu imatiphunzitsa chiyani za mphamvu ya [illegible]ulungu?

______________________________

______________________________

11. Kodi kucheza kwa Yesu ku Yerusalemu komwe anakacheza ali ndi zaka khumi ndi ziŵiri kumatiphunzitsa chiyani?

(1) ______________________________

(2) ______________________________

12. Kodi Yohane Mbatizi anali kuuza anthu kuti achite chiyani pokonzekera Khristu, iye asanaŵabatize?

______________________________

______________________________


13. Kodi Yohane Mbatizi akutiphunzitsa ife kukhala mboni zotani potsata chitsanzo cha umboni wake?

______________________________

______________________________

==========================================================================

Dziko la Israel pa Nthaŵi ya Khristu



14. Pamapu oyang'anana ndi tsamba ili, lembani dzina la dera la Israeli lililonse.

==========================================================================

MAFUNSO OCHOKERA MU SABATA LACHITATU:

15. Yesu sanabatizidwe ndi chifukwa chofanana ndi chathu. Kodi ndi chiyani chinali chosiyana pa moyo wa Yesu chomwe chimapanga ubatizo wake kukhala wosiyana?

_______________

_______________

17. Lembani za munthu aliyense wa mwa Atatuŵa momwe anaonetsedwera pa ubatizo wa Yesu.

(1) Kodi Mulungu Atate anaonetsedwa motani? _______________

_______________

(2) Kodi Mulungu Mwana anaonetsedwa motani? _______________

_______________

(3) Kodi Mulungu Mzimu Woyera anaonetsedwa motani?

_______________

18. Kodi ndi mayesero atatu otani amene Satana anaŵabweretsa kwa Yesu?

(1) _______________

(2) _______________

(3) _______________

19. Kodi ndi zinthu ziŵiri zotani zimene tiyenera kumachita kuti tigonjetse mayesero?

(1) _______________

(2) _______________

==========================================================================

SABATA LACHINAYI: KHRISTU AYAMBA NTCHITO YAKE
TSIKU LOYAMBA: CHOZIZWITSA CHOYAMBA CHOMWE CHINAPANGA OPHUNZIRA KUTI AKHULUPIRIRE

1. Sabata lapita tinaphunzira mayesero a Yesu kuti atangotha kuyesedwa anayamba ntchito yake. Sabata ino tiona zinthu zimene Iye anayamba kuchita. Koma tiyeni tizikumbukira kuti mayesero a Yesu akhoza kutithandiza.

Kodi ndi zinthu ziti zimene tiyenera kuchita kuti tigonjetse mayesero?

(1) ____________________

(2) ____________________

==========================================================================

2. Tiyenera kupempha Yesu kuti atithandize. Ndipo tiyenera kugwiritsa ntchito Mawu a Mulungu. Yesu akhoza kutithandiza chifukwa chakuti Iye mwini anayesedwa.

Yesu atangotha kuyesedwa anayamba ntchito yake. Iye anayamba kuphunzitsa ndi kuchita zozizwitsa. Zozizwitsa ndi zinthu zodabwitsa zimene munthu sangathe kuchita. Zozizwitsa zimenezi ndi zimene zinaonetsa kuti Iye anali yani? Izo zinathandiza anthu kuti amumvere Iye ndi kumukhulupirira. Tiyeni tiziphunzire m'njira iyi:

(1) Yesu anachita zozizwitsa zazikulu kuonetsa kuti Iye ndi Mwana wa Mulungu.

(2) Chozizwitsa choyamba ndicho kusandutsa madzi kukhala vinyo.

(3) Chozizwitsa choyambachi chinapangitsa ophunzira ake kuti amukhulupirire.

Tsopano tengani Buku Lopatulika kuti muone zomwe zinachitika ku Kana. Werengani Yohane 2:1 mpaka 11. Kodi Yesu ndi akuphunzira ake anapita kuti ku Kana?

____________________

==========================================================================

3. Iwo anapita ku ukwati. Mariya, mayi wake wa Yesu, anali kumeneko ndipo Yesu anaitanidwanso komweko. Pamene Yesu anabwera kuchokera kokayesedwa, poyamba Iye anapita kwa Yohane Mbatizi. Pamene Yohane anamuona anauza anthu za Yesu kuti ndiye ndani.

Yohane 1:36-37:

Ndipo poyang'ana Yesu alikuyenda, nati, "Onani Mwana wankhosa wa Mulungu! ndipo akuphunzira aŵiriwo anamva iye alikulankhula, natsata Yesu.

Zionetsa kuti ophunzira ameneŵa anali Yohane ndi Andreya. Andreya anapita kukatenga Petro mbale wake. Tsiku lina Filipo ndi Natanieli anatsatiranso Yesu. Choncho Yesu anali ndi ophunzira asanu pamene anapita ku ukwati wa ku Kana.

Pamene Yesu ndi akuphunzira ake anali pa ukwatipo panali vuto. Kodi panali vuto lotani? ____________________

____________________

==========================================================

4. Vuto linali lakuti vinyo anatha ndipo panalibenso vinyo wina amene akadapatsa anthu. Mariya anadza kwa Yesu nati, "Anthu alibe vinyo." Mariya anadziŵa kuti Yesu anali yani. Iye anadziŵa kuti ali nayo mphamvu yothandiza pa mavuto.

Poonjezera kuti ndi mwana wake, kodi Mariya anadziŵa kuti Yesu anali mwana wayani? ____________________

==========================================================

5. Mariya anadziŵa kuti Yesu anali Mwana wa Mulungu. Komanso Iye anali mwana wake. Iye mwina anadabwa ndi njira imene Yesu anamuyankhira.

Yohane 2:4:

Yesu ananena naye, "mkazi, ndili ndi chiyani ndi inu? Nthaŵi yanga siinafike."

Yesu nthaŵi imeneyi sanamutche mayi wake. Iye anati, "mkazi ." Yesu anaonetsa Mariya kuti amaganiziranso za Iye monga mwana wake. Yesu anali Mwana wa Mulungu. Mariya sayeneranso kumadza kwa Yesu kuti achite zinthu. Komabe ngakhale zinali choncho Yesu anakonza zamavuto apa ukwatiwo. Iye anasandutsa madzi kukhala vinyo.

Zozizwitsa za Yesu zidaonetsa kanthu kena kapadera kwa Iye. Kodi zimaonetsa kuti Iye ndi ndani?

---

6. Zidaonetsa kuti Yesu anali Mwana wa Mulungu. Mariya adayenera kukumbukira kuti Yesu ndi mwana wa yani? Ifenso tiyenera kukumbukira chimenechi. Yesu ananena kwa Mariya kuti, "nthaŵi yanga siinafike." Pamene Yesu anagwiritsa ntchito mawu akuti, "nthaŵi yanga," anali kutanthauza za imfa yake. Mwina Mariya anaganiza kuti Yesu adzionetse yekha monga Mesiya panthaŵi imeneyi. Yesu anamyankha kuti nthaŵi ya zimenezi siinafike. Nthaŵi imeneyi idzafika pamene Iye adzafere pa mtanda.

Yesu sanadzionetse yekha monga Mesiya pa nthaŵi imeneyi. Koma Iye anachita zinthu zimene zinaonetsa kuti Iye ndi Mwana wa Mulungu. Kodi Yesu anachita chiyani chomwe chinaonetsa kuti Iye ndi Mwana wa Mulungu?

---

7. Yesu anachita zozizwitsa. Chimenechi chidaonetsa kuti Iye ndi Mwana wa Mulungu. Chodabwitsa chake choyamba chinachitikira pa ukwati. Ngakhale zinali choncho kuti analankhula kwa Mariya monga mkazi, Mariya anadziŵa kuti Iye akhoza kuthandiza. Iye anauza otumikira kuti achite chilichonse chomwe Yesu anene. Yesu anauza otumikirawo kuti adzaze mitsuko isanu ndi umodzi yaikuluikulu ndi madzi. Mtsuko uliwonse unali kudzaza madzi oposa 100 galoni. Ndipo Yesu anauza otumikirawo kuti atunge madziwo ndi kupereka kwa mtsogoleri wa paukwatiwo.

Kodi chinaoneka ndi chiyani pamene anapatsa madziwo kwa mkulu wa phwandolo?

---

8. Madzi anasanduka vinyo. Mtsogoleriyo atalaŵa madziwo anaona kuti sanali madzinso ayi koma vinyo wokoma kwambiri. Madzi onse amene anali m'mitsuko isanu ndi umodzi anali vinyo!

Kodi ndi ndani anachita zozizwitsa zotere kuonetsa kuti Iye anali Mwana wa Mulungu?

_______________________________

===============================================================

9. Yesu ndiye amene anachita zimenezi. Chimenechi chinali chozizwitsa chake choyamba chimene chinaonetsa ulemerelo ndi mphamvu yake. Chinaonetsa kuti Iye ndi Mwana wa Mulungu.

Yohane 2:11:

> Chiyambi ichi cha zizindikiro zake Yesu anachita m'kana wa m'Galireya, naonetsera ulemerero wake; ndipo akuphunzira ake anakhulupirira Iye.

Kodi chodabwitsa choyamba chimene Yesu anachichita ndi chotani?

_______________________________

===============================================================

10. Pa chozizwitsa chake choyamba, Yesu anasandutsa madzi kukhala vinyo. Buku Lopatulika limatcha chozizwitsa chimenechi kuti ndi chizindikiro. Chimationetsa za kanthu kena kapenanso kutiganizitsa za kanthu kena. Masiku anonso timagwiritsa ntchito zizindikiro. M'mbali mwa misewu yathu ya magalimoto muli zizindikiro. Zizindikiro zimenezi zimationetsa za kanthu kena. Zimaonetsa za njira ya mumzinda. Mwina zimationetsa ife za kukhota kwa msewu. Zizindikiro zimationetsa ife kanthu kena. Kusandulika kwa madzi kuti akhale vinyo chinali chizindikiro chimene chidaonetsa kanthu kena za Yesu.

Kodi ndi zinthu zazikulu zotani zimene Yesu anachita m'moyo mwake zomwe zinaonetsa kuti Iye ndi Mwana wa Mulungu?

_______________________________

===============================================================

11. Yesu anachita zozizwitsa. Iye anachita zambiri mwa izo. Zizindikiro zonsezi zimationetsa kanthu kena za Yesu. Izo zimationetsa kuti Yesu ndi Mwana wa Mulungu. Yesu anachita zozizwitsa zosiyanasiyana. Iye anachiritsa anthu. Iye anatulutsa ziwanda. Iye anautsa anthu kwa akufa. Zodabwitsa zimenezi zimaonetsa mphamvu ya Yesu. Iye anali ndi mphamvu ya Mulungu chifukwa anali Mwana wa Mulungu. Zozizwitsa zimenezi zimaonetsa kuti Yesu ndi Mwana wa Mulungu.

Kodi chodabwitsa choyamba chimene Yesu anachita chinali chotani?

______________________________

==============================

12. Chozizwitsa choyamba chinali kusandutsa madzi kukhala vinyo. Mtsogoleri wa phwando la ukwati anadabwa. Iye sanadziŵe zomwe zinachitika. Otumikira anali odabwanso kwambiri. Ophunzira anali kudabwa kwambiri. Iwo anadziŵa zomwe zinachitika. Taonaninso ndimeyi.

Luka 2:11:
Chiyambi ichi cha zizindikiro zake Yesu anachita m'kana wa Galireya naonetsera ulemerero wake; ndipo akuphunzira ake anakhulupirira Iye.

Kodi akuphunzira anachita chiyani kwa Yesu ataona chozizwitsa choyambacho?

______________________________

==============================

13. Iwo anakhulupirira mwa Yesu. Iwo anakhulupirira kuti Iye ndi Mwana wa Mulungu. Yesu anasandutsa madzi kukhala vinyo. Chimenechi chinali chiyambi cha ntchito yake yaikulu. Iye anachita zinthu zodabwitsa zambiri atatha chimenechi.

Kodi ndi zinthu zazikulu zotani zimene Yesu anachita pa nthaŵi ya moyo wake zomwe zinaonetsa kuti Iye ndi Mwana wa Mulungu?

______________________________

______________________________

==============================

14. Yesu anachita zozizwitsa. Zozizwitsazi zinaonetsa kuti Iye ndi Mwana wa Mulungu. Buku Lopatulika limanena kuti akuphunzira anakhulupirira mwa Iye. Kodi iwo anakhulupirira chiyani? Iwo anakhulupirira kuti Yesu ndi Mwana wa Mulungu. Zimenezi zikutanthauza kuti Iye ndi Mulungu. Anthu ena amanena kuti tonsefe ndife ana a Mulungu. M'njira yakuti anatilenga ndi zoona. Koma ambiri anatembenuka kuchokera kwa Mulungu. Ena anamulandira Iye. Buku Lopatulika limatcha Akhristu ameneŵa kuti ndi ana a Mulungu. Komabe iwo sali ana a Mulungu monga mmene Yesu ali. Yesu amatchedwa Mwana "yekhayo" wa Mulungu. Chimenechi chikutanthauza kuti Iyenso ndi Mulungu.

Kodi ndi chodabwitsa chotani chimene Yesu anachita chomwe chinapangitsa ophunzira ake kuti amukhulupirire Iye?

__________________________________________________________

================================================================

15. Yesu anasandutsa madzi kukhala vinyo. Chimenechi chinakhala chozizwitsa chake choyamba. Kuchokera pa nthaŵi imeneyo Iye anachita zozwitsa zina zambiri.

Kodi chozizwitsa choyamba cha Yesu chinapangitsa ophunzira kuchita chiyani?

================================================================

16. ChinaŵWapangitsa kuti akhulupirire mwa Iye. Ifenso timakonda kumva zozizwitsa za Yesu. Ndi chinthu chodabwitsa kudziŵa zomwe Iye anachita. Chikadakhala chodabwitsa kuona madzi atasanduka vinyo. Koma kumbukirani mawu a Yesu.

Yohane 20:29:

> Yesu ananena kwa iye, chifukwa wandiona Ine, wakhulupirira; odala iwo akukhulupirira angakhale sanandiona.

Ophunzira anakhulupirira mwa Yesu monga Mwana wa Mulungu. Kodi inu mumakhulupirira kuti Yesu ndi Mwana wa Mulungu?

================================================================

17. Kodi ndi zinthu zazikulu zotani zimene Yesu anachita panthaŵi ya moyo wake zomwe zinaonetsa kuti Iye ndi Mwana wa Mulungu?

Kodi chozizwitsa choyamba cha Yesu chinali chiyani?

Kodi chozizwitsa cha Yesu choyambachi chinapangitsa ophunzira kuchita chiyani?

______________________________

==========================================================================

SABATA LACHINAYI: KHRISTU AYAMBA NTCHITO YAKE
TSIKU LACHIŴIRI: YESU ANAUZA NIKODIMO ZA KUBADWANSO KWATSOPANO

1. Kumbukirani phunzira ladzulo.

Kodi ndi zinthu zazikulu zotani zimene Yesu anachita pa nthaŵi ya moyo wake zomwe zinaonetsa kuti Iye ndi Mwana wa Mulungu?

________________________________________

Kodi chozizwitsa choyamba chimene Yesu anachita chinali chiyani?

________________________________________

Kodi chozizwitsa cha Yesu choyamba chinapangitsa ophunzira kuchita chiyani?

________________________________________

---

2. Yesu anachita zozizwitsa zomwe zinaonetsa kuti Iye ndi Mwana wa Mulungu. Chozizwitsa chake choyamba chinali chosandutsa madzi kukhala vinyo. Chozizwitsa chimenechi chinaŵapangitsa ophunzira ake kumukhulupirira Iye. Utatha ukwati wa ku Kana, Yesu anapita ku Kapernao. Iye anakhala kumeneko kwa masiku ochepa. Ndipo Iye anapita ku Yerusalemu ku phwando la paskha. Mu Yerusalemu munthu wotchedwa Nikodemo anadza kwa Yesu. Tiphunzira zinthu zimenezi kuchokera pa zimene Yesu ananena kwa Nikodemo.

(1) Tiyenera kubadwanso kwatsopano kuti tiloŵe mu ufumu wa Mulungu wa kumwamba.

(2) Pa kubadwa kwatsopano Mzimu Woyera amatipatsa moyo wa uzimu.

Tsopano tengani Buku Lopatulika ndi kuwerenga pa Yohane 3:1 mpaka 8. Ŵerengani pa ndime 3. Kodi Yesu ananena kuti aliyense adzaona ufumu wa Mulungu?

____________________

---

3. Iye sananene zimenezo. Iye ananena kuti okhawo amene abadwanso kwa tsopano adzamuona. Nikodemo anadza kwa Yesu usiku. Mwina iye anali

wotanganidwa kapena anali kuchita mantha. Iye analankhulana ndi Yesu. Yesu anauza Nikodemo mmene munthu angalowere ufumu wa Mulungu. Iye anamuphunzitsa kuti munthu ayenera kubadwanso kwatsopano kuti alowe mu-ufumu.

Kodi chinali chinthu chokwanira kwa Nikodemo kukhala mtsogoleri ndi mphunzitsi wa anthu? ________________________________

Kodi inu mukufuna kulowa ufumu wa Mulungu? ____________________

================================================================

4. Ife, monga Nikodemo, timafuna kukalowa kumwamba. Koma sikunali ko-kwanira kwa Nikodemo kungokhala mtsogoleri. Nikodemo anali Mfalisi. Afalisi anali gulu la anthu apadera. Iwo anali kuyesetsa kwambiri kuma-sunga malamulo a m'Chipangano Chakale. Iwo anali kuyesetsa kukhala ndi miyoyo yoyera. Iwo anali kumaonjezera malamulo ena ambiri pofuna kudzi-thandiza okha kuti asachimwe. Nikodemo anali munthu wotero. Iye anali wolamulira wa Ayuda. Iyeyu anali chiwalo cha bungwe la Saduki. Asaduki anali ofunika koposa. Koma iye anayenera kubadwanso kwatsopano.

Kodi Yesu anati tiyenera kubadwanso mwatsopano kuti tikalowe ufumu uti?

________________________________________________________

================================================================

5. Tiyenera kubadwanso mwatsopano kuti tikalowe ufumu wa Mulungu. Nikodemo sanafunse kuti angalowe bwanji, koma Yesu anadziwa mtima wake. Iye anamvetsetsa zomwe Nikodemo anafuna. Nikodemo anati iye anadziwa kuti Yesu anachokera kwa Mulungu chifukwa cha zozizwitsa.

Yohane 3:3:

> Yesu anayankha nati kwa iye; "Indetu, indetu, ndinena ndi iwe, ngati munthu sabadwa mwatsopano, sakhoza kuona ufumu wa Mulungu."

Kuchokera m'ndime imeneyi, kodi ndi ndani anauza Nikodemo kuti tiyenera kubadwanso kwatsopano kuti tikalowe Ufumu wa Mulungu?

______________

================================================================

6. Yesu ndiye anamuuza zimenezi. Nikodemo anali atamva kale za Yesu. Iye anamva za zozizwitsa zake. Nikodemo anafuna kutsata Mulungu. Iye ànaganiza kuti Yesu akhoza kumuuza za Mulungu. Mwina Iye anaganiza kuti Yesu akadamuuza malamulo ena ambiri oyenera kuŵasunga. Koma chimenechi sichimene Yesu ananena.

Kodi Yesù ananena kuti chiyenera kuchitika n'chiyani kwa ife tisanaloŵe muufumu wa Mulungu?

______________________________

==================================================================

7. Yesu ananena kuti ife tiyenera kubadwanso kwatsopano. Yesu anabwera kudzapereka moyo watsopano ku dziko lapansi. Iye anabwera kudzatiuza mmene tingalandirire moyo watsopanowu. Koma Nikodemo anali ndi mafunso ambiri. Iye anali kuganizira za kubadwanso kwake koyamba. Iye anali kuganiza za kubadwa kwake kwa thupi lake.

Yohane 3:4:

> Nikodemo ananena kwa Iye, "munthu akhoza bwanji kubadwa atakalamba? Kodi akhoza kulowanso m'mimba ya amake ndi kubadwa?

Kodi Nikodemo anamvetsa zimene zimachitika pa kubadwanso kwatsopano?

______________________________

==================================================================

8. Nikodemo sanamvetsetse chifukwa njira yake ya kutsata Mulungu inali yosunga malamulo. Iye sanaone mmene akadasinthikira. Iye anaganiza kuti Yesu anali kulankhula za njira imene khanda limabadwira. Koma Yesu anali kulankhula za mzimu wa munthu. Anthu ena amaganiza kuti munthu amakhala ndi moyo wauzimu pa nthaŵi imene akufa. Koma Yesu anati munthu akhoza kukhala ndi moyo wa uzimu ngakhale tsopano.

Kodi Yesu anati chiyenera kuoneka ndi chiyani tisanaloŵe muufumu wa Mulungu?

______________________________

==================================================================

9. Ife tiyenera kukhala obadwanso kwatsopano kuti tiloŵe ufumu wa Mulungu. Ife tiyenera kulandira kubadwanso kwatsopano. Nikodemo anali kuganiza za njira imene khanda limabadwira. Koma Yesu anali kulankhula za kubadwa kwa uzimu. Iye anali kulankhula za kubadwa komwe kumachitika mumtima mwa munthu. Pakubadwanso kwatsopano, Mzimu Woyera amatipatsa moyo wa uzimu.

Kubadwa koyamba kwa munthu ndi kwa thupi. Kubadwa kwatsopano kwa munthu ndi kwa mtima ndi malingaliro ake. Kodi kubadwanso kwatsopano ndi kwa thupi kapena kwa mzimu?

______________________________

==================================================================

10. Kubadwanso kwatsopano ndi kwa mzimu. Kubadwanso kwatsopano sitiyenera kubadwanso monga khanda. Yesu anafotokoza zimenezi kwa Nikodemo.

Yohane 3:5-6:

> Yesu anayankha, "Indetu, indetu, ndinena ndi iwe, ngati munthu sabadwa mwatsopano sakhoza kuona ufumu wa Mulungu. Chobadwa m'thupi chikhala thupi, ndipo chobadwa mwa Mzimu chikhala Mzimu.

Taonetsetsani bwino pa ndime zimenezi. Pamene munthu wabadwa mwatsopano, kodi iye amabadwanso mwa yani?

______________________________

==================================================================

11. Iye ali wobadwa mwa Mzimu. Chimenechi chikutanthauza Mzimu Woyera. Yesu anati munthu ayenera kukhala wobadwa mwa madzi ndi mzimu. Ndi Mzimu Woyera amene amatipatsa kubadwa mwa uzimu.

Yohane 3:8:

> Mphepo iomba pomwe ifuna, ndipo ukumva mawu ake, koma sudziŵa kumene imuka; chotere aliyense wobadwa mwa mzimu.

Bala anali kukhala m'mudzi waung'ono. Tsiku lina iye anatembenuka mtima ndipo anabadwanso mwatsopano. Moyo wake unasinthika kotheratu. Poyamba m'mudzi mwawomo munalibe munthu amene anali kumukhulupirira m'zochita zake asanabadwenso kwatsopano. Koma tsopano ndi munthu wachikondi ndi wamtendere.

Kodi ndi moyo wotani umene Mzimu Woyera anamupatsa iye pa kubadwa kwatsopano? Kodi unali wa dziko lapansi kapena wa uzimu?

________________________________________

==========================================================================

12. Mzimu Woyera anamupatsa moyo wa uzimu. Mzimu Woyera anamusintha Iye amagwira ntchito m'miyoyo yathu. Iye amatipatsa moyo wa uzimu komanso moyo wabwino umene tinalibe ndi kale lonse. Kumbukirani zomwe Yesu ananena.

Yohane 3:6:

> Chobadwa m'thupi chikhala thupi, ndipo chobadwa mwa mzimu, chikhala mzimu.

Kodi Yesu ananena kuti chimayenera kuchitika ndi chiyani kwa ife tisanalowe ufumu wa Mulungu?

________________________________________

________________________________________

==========================================================================

13. Tiyenera kubadwa mwatsopano pofuna kulowa muufumu wa Mulungu. Tiyenera kukhala ndi moyo wa uzimu. Matupi athu ndi opangidwa ndi nyama. Tili ndi maso a nyama. Ndi maso amenewa tikhoza kuona zinthu zapadziko lapansi. Ife tili ndi pakamwa ndipo tikhoza kudya chakudya. Koma kuti tione choonadi cha uzimu tiyenera kukhala ndi maso a uzimu. M'malo mofuna kulandira chakudya cha uzimu tiyenera kukhala ndi pakamwa pa uzimu. Tikhoza kukhala ndi maso ndi pakamwa pa uzimu ngati tili ndi moyo wa uzimu. Kukhala ndi moyo wa uzimu tiyenera kukhala obadwa kwatsopano.

Kuchokera ku mawu a Yesu akwa Nikodemo, kodi ndani amatipatsa moyo wa uzimu pamene tabadwa kwatsopano?

________________________________________

==========================================================================

14. Mzimu Woyera amachita zimenezi. Iye amatipatsa ife moyo wosiyana. Pamene munthu akhala Mkhristu, kanthu kena kamachitika. Moyo wake umasinthika. Iye amasiya maganizo akale. Iye amasiya machimo ake. Amakondwera ndi zinthu za uzimu. Amafuna kuphunzira kuchokera m'Buku Lopatulika. Amafuna kuyanjana ndi Akhristu ena. Iye amafuna kukula mu-

mtima mwake.

Pamene tabadwa kwatsopano, kodi ndi moyo wotani umene Mzimu Woyera amatipatsa?

________________________________________

==================================================================

15. Iye amatipatsa moyo wa uzimu. Tili obadwa kwatsopano. Anthu amayesa kulowa ufumu wa Mulungu m'njira zosiyana. Ena ali kuyesa kulowa mwa Mulungu kupyolera mwa ntchito zawo zabwino. Ena amayesa mwa kupita ku Tchalitchi. Anthu ena amaganiza kuti iwo akhoza kugula njira ya Ufumu wa Mulungu. Kotero iwo amapereka ndalama zambiri ku tchalitchi. Njira imodzi yokha yolowera mu Ufumu wa Mulungu ndi ya kubadwa kwatsopano.

Kuchokera ku Mawu a Yesu akwa Nikodemo, kodi chimachitika ndi chiyani kwa ife pa kubadwa kwatsopano?

________________________________________

==================================================================

16. Pakubadwa kwatsopano, Mzimu Woyera amatipatsa ife moyo wa uzimu. Ichi ndi chinthu chodabwitsa kwambiri. Iyi imakhala nthawi yabwino kwambiri pamene tabadwanso. Munthu aliyense padziko lapansi ayenera kukhala ndi kubadwa kumeneku.

Kodi inu munabadwa kwatsopano mwa Mzimu Woyera mwa Mulungu?

________________________________________

==================================================================

17. Tidzakambirana za zimenezi tonse pamodzi.

Mu Yohane 3, kodi Yesu anati ndi chiyani chiyenera kuoneka kwa ife tisanalowe muufumu wa Mulungu?

________________________________________

________________________________________

Kuchokera ku Mawu a Yesu a kwa Nikodemo, kodi ndi chiyani chimachitika kwa ife pa kubadwa kwatsopano? ______________________________

______________________________

========================================================================

SABATA LACHINAYI: KHRISTU AYAMBA NTCHITO YAKE
TŜIKU LACHITATU: IYE ANAUZA NIKODEMO ZA MOYO WOSATHA

1. Dzulo tinaona mmene Yesu anayamba kulankhulana ndi Nikodemo.

Mu Yohane 3, kodi Yesu anati chimayenera kuchitika ndi chiyani kwa ife tisanalowe mufumu wa Mulungu?

________________________________________

____________________________________________

Kuchokera ku Mawu a Yesu kwa Nikodemo, kodi ndi chiyani chimachitika kwa ife pa kubadwa kwatsopano?

________________________________________

_______________________________________________________

=================================================================

2. Yesu anaphunzitsa kuti munthu ayenera kubadwanso kwatsopano mmalo moti akalowe mu Ufumu wa Mulungu. Iye ananena kuti pakubadwa kwatsopano Mzimu Woyera amatipatsa moyo wa uzimu. Nikodemo anafunsa mafunso. Yesu anapitiriza kulankhulana naye. Lero tiphunzira zambiri zochokera m'mawu a Yesu.

(1) Aliyense amene amakhulupirira mwa Yesu amalandira kubadwa kwatsopano ndi moyo wosatha.

(2) Amene sakhulupirira adzafa.

Tsopano tengani Buku Lopatulika ndi kuwerenga za zimenezi mu Yohane 3:7 mpaka 18. Kodi Nikodemo anamvetsetsa mosavuta zomwe Yesu anali kunena?

__________________________________________________________

=================================================================

3. Nikodemo sanamvetsetse. Iye anafunsa kuti "Izi zingatheke bwanji? Yesu anamufotokozera kuti Mzimu Woyera amapereka kubadwa kwatsopano. Kubadwa kwatsopano ndi moyo wa uzimu operekedwa ndi Mzimu Woyera. Yesu anafotokoza kuti aliyense amene amakhulupirira mwa Iye amalandira kubadwa kwatsopano.